Kodi Ndi Citenji Kuti Ndi Pulumuke?

Ndicitenji kuti ndipulumuke? Kodi munafunsapo funso lotere? Ngati simunafunsepo, funsani! Ndifunso lalikuru limene **mukhoza** kufunsa! Yankho ya funso lakuti "Ndicitenji kuti ndipulumuke?" ndiyankho yofunikira ndithu. Sitingathe kufunsa munthu ali yense kuti atiyankhe funsoli. Baibolo ndilo buku lokha limene tikhoza kupezamo yankho yace. Tiyeni tisanthule mu malemba kuti tione anthu ouzidwa ndi Mzimu wa Mulungu m'mene anauzira anthu kucita mwakuti apulumutsidwe. Ifenso tidzaziwa cofunikira ife kucita.

Tsiku La Pentekoste

Pa tsiku la Pentekoste, kucokera pamene Kristu anakwera kunka ku Mwamba, Petro analalikira Uthenga woyamba. Analalikira za Yesu Kristu. Anauza anthu kuti Kristu anafera macimo awo. Pamene Petro anatha kulalikira, anthu anati, *"Tidzacita ciani, amuna inu, abale?"* (Macitidwe 2:37) Anthuwa anamvera za Yesu Kristu. Anakhulupirira zimene anamvera. Anatsimikiza kuti iwo anali anthu amacimo. Petro anawauza, *"Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Wotera."* (Macitidwe 2:38) Iyi inali yankho yapafupi ya Petro kufunso ya anthu yakuti "Ticitenji kuti tipulumuke?" Anakhulupirira kale zimene Petro anakamba za Yesu. Petro anawauza kuti alape ndi kubatizidwa. Akatero, iwo adzalandira cikhululukiro ca macimo awo. Tiyenera kulapa macimo athu ndi ku batizidwa. Tikatero, macimo athu akhululukidwa.

Mdindo Wa Ku Aitiopiya

Mu Macitidwe 8:26-40 tiuzidwa za ku tembenuka kwa mdindo wa ku Aitiopiya. Filipo analalikira "Yesu" kwa mdindoyo (Macitidwe 8:35). Ndipo monga anapita panjira pao, anadza ku madzi. Ndipo mdindoyo anati, *"Taonapo madzi; cindiletsa ine ciani ndisabatizidwe?"* (Macitidwe 8:36) Filipo anamuuza ngati iye akhulupirira ndi mtima wace wonse, akhoza kubatizidwa. Ndipo mdindo anayankha, *"ndikhulupirira kuti Yesu Kristu ndi Mwana wa Mulungu"* (Macitidwe 8:37). Ndipo anatsikira onse awira ku madzi, Filipo ndi mdindoyo. Ndipo Filipo anambatiza iye. Apa tiona kuti mdindo anamvera kulalikidwa za Yesu. Anakhulupirira kuti Yesu Kristu ndi Mwana wa Mulungu. Anabvomelekeza cikhulupiriro cace mwa Kristu. Pambuyo pace, anabatizidwa.

Saulo Wa Ku Tariso

Kutembenuka kwa Saulo wa ku Tariso (Pambuyo pace Mtumwi Paulo) ku kambidwa mu Macitidwe Mutu 9, 22, ndi 26. Saulo anali pa njira pace kupita ku Damasiko ku ka manga a Kristu. Ndipo poyenda ulendo wace, anakanthidwa ndi khungu osapenya kanthu. Kristu anaonekera kwa iye. Anauza Saulo, *"Uka, nulowe m'mudzi, ndipo kudzanenedwa kwa iwe cimene uyenera kucita"* (Macitidwe 9:6). Saulo anacita cimene anauzidwa kutcita. *"Ndipo tsopano ucedweranji? Tauka, nubatizidwe ndi kusamba kucotsa macimo ako, nuitane pa dzina lace"* (Macitidwe 22:16). Kucita ciani? Anauzidwa kuti auke ndi kubatizidwa. Cifukwa? Kuti asambe kucotsa macimo ace. Saulo sanakhululukidwe macimo kufikira pamene atatha kubatizidwa.

Korneliyo

Mu Macitidwe 10 ndi 11, zikamba za kutembenuka kwa Korneliyo. Korneliyo anali munthu woyamba kukhala Mkristu amene sanali mu Yuda. Korneliyo anali msilikari wa ci Roma. Baibolo ikamba kuti anali *"munthu wopembeza, ndi wakuopa Mulungu ndi banja lace lonse, amene anapatsa anthu za cifundo za mbiri, napemphera Mulungu kosaleka"* (Macitidwe 10:2). Kodi iwe ukhoza kukambidwa ndi zinthu zabwino zotere? Korneliyo anali ndithu munthu wabwino. Komabe, Korneliyo anali **wotaika**!

Macimo ace anali asanakhululukidwe! Ambuye anauza Korneliyo kuti atumize amuna ku Yopa kuitana Petro. Petro *"adzalankhula nawe mau, udzapulumutsidwa nao iwe ndi apa banja ako onse"* (Macitidwe

11:14). Petro analalikira Kristu kwa iwo. Pambuyo pace *"analamulira iwo abatizidwe m'dzina la Yesu Kristu"* (Macitidwe 10:48). Apa tiri ndi munthu (Korneliyo) amene anali munthu wa cipembedzo. Analinso munthu wa bwino. Komabe, anali munthu **wotaika wa macimo**! Macimo ace anali asanakhululukidwe. Anaitana Petro kuti amuphunzitse zinthu zakuti acite mwakuti apulumutsidwe. Petro anamuuza ndi apabanja kuti abatizidwe. Pamene atabatizidwa, anawakhululukira macimo awo.

Potsiridza

Tinayamba ndi kufunsa, "Kodi ndi citenji kuti ndipulumutsidwe?" Tinasanthura Baibolo kuti tipeze yankho ku funsoli. Mu Kuphunzira kwathu, tapeza kuti anthu **anamvera** za Yesu Kristu. Anamvera kuti Yesu anafa kuti akhululukire anthu macimo awo. Anthu **anakhulupirira** mau. Anakhulupirira kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu. Anamvetsa kuti anali otaika mu macimo awo. Anauzidwa kuti **alape** macimo awo. **Anabvomelekeza** kuti Yesu Kristu ndi Mwana wa Mulungu. Anabvomelekeza, sanakhululukidwe pamene asanabatizidwe.

Kodi ukhulupirira mwa Yesu Kristu? Unalapa macimo ako? Unabvomelekeza kuti Yesu Kristu ndi Mwana wa Mulungu? Kodi munabatizidwa kuti macimo anu akhululukidwe? Ngati simunatero, ziwani kuti mukali ndithu kukhala mu macimo anu. Muli otaika.

Landilani Uthenga lero monga anacitira anthu amacimo aja mu Baibolo. Mukatero mwai muli nao kuti mudzapulumutsidwa.

Truth For The World

truthfortheworld.org

info@tftw.org

P.O. Box 5048
Duluth, GA 30096
U.S.A.

CC BY NC ND

Kodi Ndi Citenji Kuti Ndi Pulumuke?